# Initial Primary Teacher Education

**Buku lophunzitsira**

**m'Sukulu za Uphunzitsi**

# Chichewa

**Buku loyamba**

**Chaka choyamba**

**Malawi Institute of Education**

**Buku lophunzitsira**

**m’Sukulu za Uphunzitsi**

# Chichewa

**Buku loyamba**

**Chaka choyamba**

**Omwe adalemba ndi kusindikiza bukuli**

Malawi Institute of Education
P. O. Box 50
Domasi
Malawi

Email: miedirector@sdnp.org.mw
Website: www.mie.edu.mw

©Malawi Institute of Education 2017

Zonse zam'bukumu n'zosati munthu akopere munjira ina iliyonse popanda chilolezo. N'zosatinso munthu achitire malonda mpang'ono pomwe. Komabe ngati munthu afuna kugwira ntchito yazamaphunziro ndi bukuli, ayambe wapempha ndikulandira chilolezo kuchokera kwa eniake omwe adalisindikiza.

Kusindikiza koyamba kwa bukuli 2017

## Olemba

| | |
|---|---|
| Innocencia Guzako-Kachala | Lilongwe Teachers' College |
| John Kunkumbira | St Joseph's Teachers College |
| Gertrude Mkandawire | Blantyre Teachers' College |
| Laston Mkhaya | Montfort Special Needs College |
| Ndamyo Mwanyongo | Kasungu Teachers' College |
| Wisdom Nkhoma | Domasi College of Education |

## Kuthokoza

Unduna wa za Maphunziro, Sayansi ndi Luso pamodzi ndi Malawi Institute of Education akuthokoza anthu onse amene adathandiza mu njira zosiyansiyana kuti bukuli lilembedwe.

Akuthokoza makamaka bungwe la UNICEF ndi GIZ chifukwa cha thandizo la chuma ndi upangiri osiyanasiyana pa nthawi yolemba bukuli.

Undunawu ukuthokozanso mwapadera Mkulu wa Department of Inspectorate and Advisory Services (DIAS), a Raphael Agabu, ndi onse ogwira ntchito ku Dipatimentiyi, Mkulu wa Malawi Institute of Education, Dr William Susuwele-Banda, ndi onse ogwira ntchito kumeneko, Mtsogoleri wa ntchito yokonzanso maphunziro a m'sukulu za uphunzitsi (IPTE), Dr Ezekiel Kachisa ndi onse owathandizira (a Edward G Mtonga ndi Catrin Anderer) chifukwa chotsogolera ntchito yolemba bukuli.

A MIE ndi Undunawu akuthokozanso a Frackson Manyamba, Foster NJ Gama, Benjamin David, Margret Mandala-Bandason, Margaret Magalasi ndi Bernadetta Namangale-Jere pounikira bukuli ndi kupereka malangizo othandiza

**Okonza**

**Mkonzi** : Max J Iphani

**Wotayipa** : Anastazia T Mbungulo
**Mkonzi wamkulu** : Max J Iphani

## Mawu otsogolera

Maphunziro ndi maziko a chitukuko m'dziko. Iwo ndi gwero la chitukuko pa moyo wa munthu, gulu la anthu ngakhalenso dziko. Maphunziro amakonzekeretsa ophunzira kukhala ndi maluso oti azithandiza kutukula moyo wa anthu ndi chuma cha dziko moyenera. Makolo amafuna kuti ana awo azikula ndi nzeru zabwino komanso moyo wathanzi kudzera m'maphunziro, omwe angawathandize kukhala ndi maluso ndi maganizo abwino kuti akhale anthu odalirika ndi a moyo wokondwa.

Choncho n'koyenera kuti maphunziro azikhala othandiza ophunzira kukhala a makhalidwe abwino, maganizidwe oyenera komanso odziwa udindo wawo. Chotero ophunzira uphunzitsi aziphunzitsidwa moyenera kuti azitha kuphunzitsa mwaluso.

Pali zinthu zambiri zimene zimathandiza kuti maphunziro akhale apamwamba. Chimodzi mwa izo ndi kukhala ndi aphunzitsi osulidwa bwino. Aphunzitsi ali ndi gawo lalikulu pophunzitsa chifukwa ndiwo amatsogolera ophunzira kupeza nzeru za maphunziro. Iwo amakhalanso chitsanzo kwa ophunzira m'machitidwe awo.

Cholinga cha maphunziro a zauphunzitsi m'Malawi ndi kusula aphunzitsi ogwira ntchito yawo mwaluso ndi mwaukadaulo. Izi zimatheka ngati aphunzitsiwa aphunzitsidwa mwaluntha kuti akhale ndi nzeru, maluso ndi ukadaulo wowathandiza kuphunzitsa ophunzira akupulayimale moyenera. Choncho maphunziro a uphunzitsi a IPTE aunikidwanso ndi cholinga choti ophunzira uphunzitsi akamatsiriza maphunziro awo azikhala atasulidwa mwaluso kuti akagwire ntchito yawo mwaukadaulo.

Ndondomeko younikanso maphunzirowa yatsogoloeredwa ndi lingaliro ili:

'Kusula mphunzitsi wodziunika, wodzidalira, wozindikira kuti kuphunzira sikutha pa moyo wa munthu, wamakhalidwe abwino komanso wodziwa kuphunzitsa ophunzira osiyanasiyana molingana ndi kuthekera kwawo.'

Tikukhulupirira kuti sukulu zophunzitsa ntchito yauphunzitsi m'Malawi muno zizindikira kuti maphunzirowa ndi aphindu pothandiza ophunzira uphunzitsi kukhala ndi maziko odalirika a ntchito yawo.

Executive Director

Malawi Institute of Education

## Zam'katimu


| | | |
|---|---|---|
| Kuthokoza | ……………………………………………………..……… | v |
| Mawu otsogolera | ……………………………………………………….. | vi |
| Mutu 1 | Kufunika kwa phunziro la Chichewa……………….. | 1 |
| Mutu 2 | Silabasi, buku la mphunzitsi ndi la ophunzira…..….. | 3 |
| Mutu 3 | Kaphunzitsidwe ka kumva ndi kuyankhula…….… | 6 |
| Mutu 4 | Kaphunzitsidwe ka kuwerenga………………………. | 10 |
| Mutu 5 | Kaphunzitsidwe ka kuwerenga (kupitiriza)………... | 15 |
| Mutu 6 | Kaphunzitsidwe ka kukonzekera kulemba…………. | 19 |
| Mutu 7 | Kuphunzitsa mitundu ya kulemba………………….. | 23 |
| Mutu 8 | Kulemba dongosolo la ntchito……………………… | 25 |
| Mutu9 | Kulemba chikonzekero cha phunziro……………… | 31 |
| Mutu 10 | Kulemba zotsatira za ntchito yomwe ndaphunzitsa.. | 37 |
| Mutu 11 | Kaphunzitsidwe ka malamulo a chiyankhulo…… | 39 |
| Mutu 12 | Kaphunzitsidwe ka ndagi, nthano ndi sewero……… | 43 |

# MUTU1 Kufunika kwa phunziro la Chichewa

**Luso:** **Kumva ndi kuyankhula**
**Nthawi:** **Maola 1**
**Chigawo:** **Choyamba**

## Chiyambi

Chiyankhulo chimayambira pa kumva maliwu omwe wina akuyankhula. Wakumva amayankha zomwe wamvazo. Zinthu zomwe timamva ndi kuziyankhula timatha kuziphunzira m'mabuku powerenga. Tikatero timalemba zomwe tamva kapena tawerenga. Poyankhula kapena polemba timaganizira zinthu mofatsirira n'cholinga choti tipereke maganizo ogwira mtima. Tikamayankhula kapena tikamalemba, timatsata malamulo a chiyankhulo.

Motero maluso a chiyankhulo ndi awa: kumva, kuyankhula, kuwerenga, kulemba, kuganiza mozama ndi kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo. Malusowa ndi omwe ophunzira ayenera kuphunzira.

M'mutu uno, muphunzira kufunika kwa phunziro la Chichewa kupulayimale ndi ku sukulu zophunzitsa ntchito yauphunzitsi (TTC).

## Zizindikiro za kakhozedwe

Pakutha pa mutu uno, ophunzira afotokoza kufunika kwa phunziro la Chichewa kupulayimale ndi ku sukulu zophunzitsa ntchito yauphunzitsi.

**Ntchito 1: Kukambirana kufunika kwa maluso a chiyankhulo**

1. Kambiranani tanthauzo la maluso a chiyankhulo.
2. Kambiranani kufunika kwa maluso a kumva ndi kuyankhula, kuwerenga, kulemba, kuganiza mozama ndi kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo.
3. Kambiranani mgwirizano womwe umakhalapo pakati pa maluso asanu ndi limodzi a chiyankhulo.
4. Fotokozerani anzanu zomwe mwakambirana.
5. Perekani maganizo anu pa zomwe anzanu afotokoza.

> **Malangi kwa mphunzitsi**
> Mupezeretu matanthauzo a maluso asanu ndi limodzi ndi zolinga za luso lililonse.

**Ntchito 2: Kufotokoza kufunika kwa phunziro la Chichewa**

1. Kambiranani zifukwa zophunzitsira phunziro la Chichewa kupulayimale ndi kusukulu zophunzitsa ntchito yauphunzitsi.
2. Fotokozerani anzanu zomwe mwakambirana.
3. Perekani maganizo anu pa zomwe anzanu afotokoza.

> **Malangizo kwa mphunzitsi**
> Mupezeretu mayankho a ntchitoyi koyambirira kwa silabasi ya Chichewa.

## Kufotokoza mwachidule

M'mutu uno mwaphunzira tanthauzo la maluso a chiyankhulo ndi kufunika kwake. Mwaona mgwirizano womwe umakhalapo pa maluso a kumva ndi kuyankhula, kuwerenga, kulemba, kuganiza mozama ndi kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo. Pomaliza, mwafotokoza kufunika kophunzitsa phunziro la Chichewa kusukulu zapulayimale ndi kusukulu zophunzitsa ntchito yauphunzitsi.

## Kudziunika ndi kudziyesa

1. Pa maluso asanu ndi limodzi a chiyankhulo, mukuganiza kuti ndi maluso anayi ati omwe ndi akuluakulu?
2. Kodi maluso ena awiriwa amathandiza bwanji maluso akuluakulu anayi a chiyankhulo?
3. N'chifukwa chiyani ophunzira ena sakonda phunziro la Chichewa?
4. Mungachite bwanji kuti ophunzira anu azikonda phunziro la Chichewa?

## Mabuku

Malawi Institute of Education (2009). *Initial Primary Teacher Education through Open and Distance Learning (ODL) Chichewa Module 1*. Domasi: MIE.

Malawi Institute of Education (2008). *Maphunziro M'sukulu Zauphunztsi m 'Malawi Buku la Mphunzitsi*. Domasi: MIE.

# MUTU 2 Silabasi, buku la mphunzitsi ndi la ophunzira

**Luso :** Kumva ndi kuyankhula
**Nthawi :** Maola 3
**Chigawo:** Choyamba

## Chiyambi

Maphunziro amayenera kukhala ndi dongosolo la ntchito yoyenera kuphunzitsa chaka chonse cha sukulu. Dongosololi limatchedwa silabasi. Limathandiza kuti pasakhale kusiyana kwa maphunziro omwe ophunzira akulandira m'sukulu zonse za m'dziko. Silabasi imasonyeza mitu ya ntchito yoyenera kuphunzitsa m'chigawo chilichonse cha sukulu.Kalasi lililonse lili ndi silabasi yake. Mitu ya m'silabasi imagwirizana ndi yomwe ili m'buku la mphunzitsi ndi m'buku la ophunzira.

Ophunzira ntchito yauphunzitsi ayenera kudziwa kuti silabasi ndiyo imatsogolera mphunzitsi zoyenera kukaphunzitsa pa mutu uliwonse komanso m'chigawo chasukulu chilichonse. N'kofunikanso kuti adziwe kufunika kwa silabasi, buku la mphunzitsi ndi la ophunzira, ndi kuzukuta ntchito zopezeka m'magawo amabukuwa.

## Zizindikiro za kakhozedwe

Pakutha pa mutu uno, ophunzira:

- afananitsa ntchito yopezeka mu silabasi ndi yomwe ili m'buku la mphunzitsi ndi la ophunzira.
- agwiritsa ntchito silabasi, buku la mphunzitsi ndi buku la ophunzira moyenera.

## Mawu otsogolera

Mphunzitsi amakonza ntchito yokaphunzitsa potenga mitu yomwe ili m'silabasi, m'buku la mphunzitsi ndi la ophunzira. Pali mitundu iwiri ya silabasi: yophunzitsira ndi yamayeso.Aphunzitsi amagwiritsa ntchito silabasi yophunzitsira.Silabasi imathandiza kuti ophunzira m'sukulu zonse aziphunzira zofanana. Silabasi ili ndi magawo asanu ndi limodzi. Magawowa ndi awa: mlingo wa kakhozedwe, zizindikiro za kakhozedwe, mutu, zina mwa zomwe ophunzira achite, zina mwa njira zophunzitsira, zophunzirira ndi zoyesera, ndi zina mwa zipangizo zophunzitsira, zophunzirira ndi zoyesera.

M'buku la mphunzitsi muli mfundo zofotokoza kufunika kwa phunziro la Chichewa, magawo akuluakulu abukuli ndi mitu ya ntchito yoti ophunzira achite. Mulinso malangizo omuunikira mphunzitsi zina zoti achite kuti phunziro liyende bwino. M'mabuku a ophunzira muli nkhani komanso ntchito yoti ophunzira achite.

Silabasi, buku la mphunzitsi ndi mabuku aophunzira zimaunikira mphunzitsi ntchito yokaphunzitsa komanso zoti ophunzira achite pamene akuphunzira. Buku la mphunzitsi amagwiritsa ntchito ndi mphunzitsi yekha. Choncho ndi bwino kuti ophunzira uphunzitsi aphunzire momwe azikagwirtsira ntchito mabukuwa pokonza

dongosolo la ntchito ndi chikonzekero cha phunziro. Akuyeneranso kudziwa kulumikizana kwa mitu ya ntchito kuyambira m'Sitandade 1 mpaka 8.

**Ntchito 1 Kufananitsa ntchito yopezeka mu silabasi ndi yomwe ili m'buku la mphunzitsi ndi la ophunzira**

1. Kambiranani tanthauzo la silabasi.
2. Unikani mwachidwi silabasi, buku la mphunzitsi ndi la ophunzira.
3. Kambiranani ntchito yopezeka m'silabasi, m'buku la mphunzitsi ndi la ophunzira.
4. Fananitsani ntchito yopezeka m'mabukuwa.
5. Siyanitsani ntchito yopezeka m'mabukuwa.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Mufufuziretu tanthauzo la silabasi powerenga mabuku ena.
- Mupezeretu masilabasi, mabuku a aphunzitsi ndi mabuku a ophunzira a Sitandade 1 mpaka 4.
- Mupempheretu chilolezo kwa mphunzitsi wamkulu wa sukulu yomwe ophunzira anu achiteko kafukufuku.

**Ntchito 2 Kufufuza momwe mphunzitsi amagwiritsira ntchito silabasi, mabuku ophunzitsira ndi ophunzirira**

1. Unikaninso mwachidwi silabasi, buku la mphunzitsi ndi la ophunzira.
2. Pitani ku sukulu yapulayimale yomwe mwayandikana nayo ndi kukafufuza momwe mphunzitsi ndi ophunzira amagwiritsira ntchito silabasi, buku la mphunzitsi ndi buku la ophunzira.
3. Perekani maganizo anu pa zomwe mwapeza.

**Malangizokwa mphunzitsi**
Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.

**Ntchito 3 Kugwiritsa ntchito silabasi, buku la mphunzitsi ndi la ophunzira**

1. Unikaninso kagwiritsidwe ntchito ka silabasi, buku la mphunzitsi ndi la ophunzira.
2. Zukutani zomwe zikupezeka m'magawo a silabasi, buku la mphunzitsi ndi la ophunzira.
3. Sonyezani momwe mungagwiritsire ntchito mabukuwa.
4. Perekani maganizo anu pa ntchito yomwe anzanu achita.

**Malangizo kwa mphunzitsi**
Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.

## Kufotokoza mwachidule

M'mutu uno mwaphunzira tanthauzo la silabasi, mwaunika ntchito zopezeka m'magawo a silabasi, buku la mphunzitsi ndi la ophunzira.

Mwafananitsa ndi kusiyanitsa ntchito yopezeka m'magawo a silabasi, buku la mphunzitsi ndi la ophunzira. Kenaka, mwafufuza momwe mphunzitsi ndi ophunzira akupulayimale amagwiritsira ntchito mabukuwa. Potsiriza, mwasonyeza momwe mungagwiritsire ntchito silabasi, buku la mphunzitsi ndi la ophunzira.

## Kudziunika ndi kudziyesa

**1** Tchulani magawo a silabasi omwe mungapezemo izi:
- bokosi la kanema
- ayankha moni molondola
- malonje
- amva malonje
- mafunso ndi mayankho
- kupatsana moni molondola

**2** Fotokozani kusiyana kwa buku la mphunzitsi ndi buku la ophunzira.

**3** Mungachite chiyani ngati pasukulu pomwe mukuphunzitsa palibe silabasi?

**4** Fotokozani kagwiritsidwe ntchito ka zipangizo zotsatirazi pophunzitsa:
- kalilole (galasi)
- bokosi la kanema
- nthenga
- zithunzi zotukuza

## Matanthauzo a mawu

**Buku la mphunzitsi:** buku lotsatira silabasi lomwe limatsogolera mphunzitsi polemba chikonzekero cha phunziro ndi pophunzitsa

**Buku la ophunzira:** buku lotsatira silabasi lomwe ophunzira amagwiritsa ntchito

## Mabuku


Malawi Institute of Education (2009).*Initial Primary Teacher Education (IPTE) through Open and Distance Learning (ODL) Chichewa module 1.*Domasi: MIE.

Malawi Institute of Education (2008). *Maphunziro M'sukulu Zauphunztsi m 'Malawi buku la mphunzitsi.* Domasi: MIE.

# MUTU 3 Kaphunzitsidwe ka kumva ndi kuyankhula

**Luso :** **Kumva ndi kuyankhula**

**Nthawi :** **Maola 5**

**Chigawo:** **Choyamba**

## Chiyambi

Mphunzitsi akuyenera kuphunzitsa maluso a kumva ndi kuyankhula moyenera. Ophunzira akaphunzira luso la kumva ndiye kuti adzakhala atcheru ndi kumvetsetsa nkhani zosiyanasiyana zomwe ena akuyankhula. Akaphunzira luso la kuyankhula adzatha kupereka maganizo awoawo kwa ena poyankhula mosakayika m'zochitika zosiyanasiyana.

Ngakhale kuti kumva ndi kuyankhula ndi maluso awiri osiyana, pophunzitsa amaphunzitsidwira nthawi imodzi. N'kovuta kuti mphunzitsi asiyanitse chifukwa kumva ndi kuyankhula kumachitika nthawi imodzi. Pamene wina akuyankhula wina amamvetsera. Izi zili chimodzimodzi m'kalasi; ophunzira amayenera amagwiritsa ntchito maluso akumva ndi kuyankhula. Mphunzitsi amadziwa kuti ophunzira amva ngati akuchita zomwe amva monga poyankha mafunso molondola.

M'mutu uno, muphunzira momwe mungaphunzitsire maluso a kumva ndi kuyankhula mu Sitandade 1 mpaka 4.

## Zizindikiro zakakhozedwe

Pakutha pa mutu uno, ophunzira:

- apeza mitu ya kumva ndi kuyankhula m'mabuku a Sitandade 1 mpaka 4.
- afotokoza mitundu ya maliwu, malonje ndi zouzidwa.
- asonyeza kaphunzitsidwe ka mitundu ya maliwu, malonje ndi zouzidwa.

## Mawu otsogolera

M'silabasi ya kupulayimale muli mitu ya ntchito ya kumva ndi kuyankhula yosiyanasiyana. Ntchito za m'mituyi zimakulitsa maluso akumva ndi kuyankhula kwa ophunzira ndi mphunzitsi. Pali njira zosiyanasiyana zomwe mphunzitsi angagwiritse ntchito pophunzitsa ntchito za kumva ndi kuyankhula. Mphunzitsi akuyenera kuzindikira mitundu, kufunika ndi ndondomeko yophunzitsira mitu ya ntchito ya kumva ndi kuyankhula kuti athandize ophunzira moyenera.

**Ntchito 1 Kufotokoza kufunika kwa maluso a kumva ndi kuyankhula**

1. Kambiranani kufunika kwa maluso a kumva ndi kuyankhula.
2. Fotokozerani anzanu zomwe mwalemba.
3. Perekani maganizo anu pa ntchito yomwe anzanu achita.

**Malangizo kwa mphunzitsi**
Mufufuziretu mfundo zosonyeza kufunika kwa maluso a kumva ndi kuyankhula.

### Ntchito 2 Kufufuza mitu ya kumva ndi kuyankhula mu Sitandade 1 mpaka 4

1 Unikani mitu ya ntchito ya maluso a kumva ndi kuyankhula m'mabuku a Sitandade 1 mpaka 4.
2 Lembani zomwe mwapeza.
3 Fotokozerani anzanu zomwe mwapeza.
4 Perekani maganizo anu pa ntchito yomwe anzanu achita.

**Malangizo kwa mphunzitsi**
Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.

### Ntchito 3 Kufotokoza njira zophunzitsira maluso a kumva ndi kuyankhula

1 Kambiranani njira zophunzitsira maluso a kumva ndi kuyanhula.
2 Lembani zomwe mwakambirana.
3 Fotokozerani anzanu zomwe mwalemba.
4 Perekani maganizo anu pa ntchito yomwe anzanu achita.

**Malangizo kwa mphunzitsi**
- Mufufuziretu zina mwa njira zophunzitsira maluso a kumva nd kuyankhula.
- Muombe mkota pa ntchito yomw ophunzira achita.

### Ntchito 4 Kufotokoza mitundu ya maliwu, malonje ndi zouzidwa

1 Kambiranani tanthauzo la maliwu, malonje ndi zouzidwa.
2 Kambiranani mitundu ya maliwu, malonje ndi zouzidwa.
3 Lembani zomwe mwakambirana.
4 Fotokozerani anzanu zomwe mwalemba.
5 Perekani maganizo anu pa ntchito yomwe anzanu achita.

**Malangizo kwa mphunzitsi**
- Mufufuziretu mitundu ya maliwu, malonje ndi zouzidwa.
- Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.

### Ntchito 5 Kufotokoza ndondomeko yophunzitsira maliwu, malonje ndi zouzidwa

1 Kambiranani ndondomeko yophunzitsira maliwu, malonje ndi zouzidwa.
2 Lembani zomwe mwakambirana.
3 Fotokozerani anzanu zomwe mwalemba.
4 Perekani maganizo anu pa ntchito yomwe anzanu achita.

**Malangizo kwa mphunzitsi**
- Mufufuziretu ndondomeko yophunzitsira maliwu, malonje ndi zouzidwa.
- Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.

**Ntchito 6 Kusonyeza kaphunzitsidwe ka mitundu ya maliwu, malonje ndi zouzidwa**

1 Unikani ndondomeko yophunzitsira maliwu, malonje ndi zouzidwa.
2 Sonyezani momwe mungphunzitsire mitu yotsatirayi:
   a mitundu ya maliwu mu Sitande 1 ndi 2.
   b mitundu ya malonje mu Sitandade 1 mpaka 4.
   c zouzidwa.
3 Perekani maganizo anu pa ntchito yomwe anzanu achita.

**Malangizo kwa mphunzitsi**
Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.

## Kufotokoza mwachidule

M'mutu uno mwaphunzira kufunika kwa maluso akumva ndi kuyankhula. Mwafufuza mitu ya ntchito zophunzitsiramaluso a kumva ndi kuyankhula mu Sitandade 1 mpaka 4. Mwafotokoza ndondomeko yophunzitsira maluso a kumva ndi kuyankhula. Pomaliza, mwasonyeza momwe mungaphunzitsire mitundu ya maliwu, malonje ndi zouzidwa.

## Kudziunika ndi kudziyesa

1 Fotokozani kufunika kwa maluso a kumva ndi kuyankhula.
2 Tchulani mitu isanu ya ntchito zophunzitsira maluso a kumva ndi kuyankhula.
3 Ndi mavuto otani omwe mphunzitsi wa Sitandade 1 amakumana nawo pophunzitsa maluso a kumva ndi kuyankhula?
4 Yerekezani kuti mukuphunzitsa liwu latsopano /dw/ m'Sitandade 1 ndipo mwawauza ophunzira kuti aziloza chala m'mwamba mukatchula mawu oyamba ndi /dw/. Koma Zondiwe waloza chala m'mwamba mutatchula mawu oti "dala". Fotokozani zomwe mungachite ndi Zondiwe.

## Matanthauzo a mawu

**Kuyankhula** kutulutsa mawu atanthauzo kudzera pakamwa

**Kumva** kulandira mawu kudzera m'makutu

## Mabuku


Department of Teacher Education and Development, (2009). *Initial Primary Teacher Education through Open and Distance Learning Chichewa (Module 1).*

Malawi Institute of Education (2016). *Malawi Primary Education Chichewa Buku la mphunzitsi la Sitandade 1.* Domasi: MIE.

Malawi Institute of Education (2008). *Maphunziro a M'sukulu Zauphunzitsi m'Malawi Buku la Mphunzitsi*. Domasi: MIE.

Malawi Institute of Education (2017). *National Reading Programme Standard 1 teacher resource handbook*. Domasi: MIE.


## Mabuku oonjezera

https://www.readnaturally.com/research/5-components-of-reading

http://www.scsk12.org/scs/subjectareas/kweb/images/nationalreadingpanel_faq.pdf

https://cehdvision2020.umn.edu/blog/helping-kids-with-reading/

# MUTU 4 Kaphunzitsidwe ka kuwerenga

**Luso :** Kuwernga
**Nthawi:** Maola 6
**Chigawo:** Choyamba

## Chiyambi

Luso la kuwerenga ndi limodzi mwa maluso ofunika m'phunziro la Chichewa. Mphunzitsi ayenera kudziwa zolinga zophunzitsira kuwerenga m'sukulu zapulayimale. Kuwerenga kumathandiza ophunzira kudziwa chiyankhulo. Ophunzira amapeza nzeru zambiri kuchokera pa zomwe akuwerenga zomwe ndi zothandiza pa moyo wawo.

M'mutu uno ndi wotsatira, muphunzira momwe mungaphunzitsire kuwerenga m'sukulu za pulayimale potsatira nsanamira zisanu za kuwerenga.

## Zizindikiro zakakhozedwe

Pakutha pa mutu uno, ophunzira:

- afotokoza za nsanamira ya kumva ndi kutchula maliwu, kuzindikira malembo ndi maliwu ake ndi nsanamira ya kuwerenga molondola, mofulumira ndi mosadodoma.
- asonyeza kaphunzitsidwe ka nsanamira ya kumva ndi kutchula maliwu, kuzindikira malembo ndi maliwu ake ndi nsanamira ya kuwerenga molondola, mofulumira ndi mosadodoma mu Sitandade 1 mpaka 4.

## Mawu otsogolera

Kuphunzitsa kuwerenga pogwiritsa ntchito nsanamira zisanu za kuwerenga kumathandiza ophunzira kuzamitsa luso la kuwerenga. Mphunzitsi ayenera kudziwa ndi kumvetsa bwino nsanamira zisanu za kuwerenga zomwe ndi zotsatirazi:

**Kumva ndi kutchula maliwu**
Ophunzira ayenera kumvetsetsa kuti mawu amapangidwa ndi maliwu. Mwachitsanzo, mawu oti "ana"apangidwa ndi maliwu awa: /a/, /n/ ndi /a/.

**Kuzindikira malembo ndi maliwu**
Ophunzira ayenera kumvetsetsa kuti malembo amaimira maliwu, ndipo mawu amapangidwa kuchokera ku malembowa. Mu Sitandade 1 muli malembo awa: a, n, i, m, u, k, o, l, e, w t, d, s, p, nd, ch, y, b, z, g, r, f, h, j, v, dz, mw, nz, kw, ts, th, mb, kh, ng, ns, mp, nj, ny, bw, mt, ph, ng', dw, ps, bz, fw, gw, ml, mv, dy, ms, sw, mk, mz ndipo mu Sitandade 2 muli malembo awa: mf, m'b, mph, nth, tch, mgw, ng'w, mch, khw, phw, mg, mm, pw, sh, zw, zy, nkh, ngw, mts, mbw, ndw, thw, thy, tsw, msw, nsw, mpw, ntch, nkhw, mphw, mtch, nthw, mtsw ndi mnkhw.

**Kuwerenga molondola, mofulumira ndi mosadodoma**
Uku ndi kuzindikira maliwu ndi mawu mosataya nthawi.

**Kudziwa mawu ndi matanthauzo ake**

Uku ndi kudziwa matanthauzo a mawu osiyanasiyana m'chiyankhulo.

**Kumvetsa nkhani**

Uku ndi kumvetsetsa nkhani yomwe munthu wamva kapena kuwerenga.

**Ntchito 1 Kufotokoza nsanamira ya kumva ndi kutchula maliwu**

1. Pezani zitsanzoza ntchito za nsanamira ya kumva ndi kutchula maliwu kuchokera m'buku la mphunzitsi ndi la ophunzira la Sitandade 1.
2. Kambiranani zitsanzozomwe mwapeza.
3. Fotokozerani anzanu zomwe mwakambirana.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Mutsogolere ophunzira kupeza zitsanzo za ntchito za nsanamira ya kumva ndi kutchula maliwu (Phonological awareness routines).
- Muonetsetse kuti mwalemberatu zitsanzo zisanu za ntchito ya nsanamira ya kumva ndi kutchula maliwu.
- Musonyeze ophunzira kachitidwe ka ntchito (routine) iliyonse.
- Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.

**Ntchito 2 Kusonyeza kaphunzitsidwe ka kumva ndi kutchula maliwu mu Sitandade 1 ndi 2**

1. Unikani ntchito za nsanamira ya kumva ndi kutchula maliwu.
2. Sonyezani momwe mungaphunzitsire ntchito za nsanamira ya kumva ndi kutchula maliwu.
3. Zukutani phunziro lililonse.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Muonetsetse kuti ophunzira akutsatira njira yoyamba ndi mphunzitsi, mphunzitsi ndi ophunzira, kenaka ophunzira paokha moyenera.
- Muonetsetse kuti muli ndi mabuku a mphunzitsi a Sitandade 1 ndi 2.

**Ntchito 3 Kufotokoza nsanamira ya kuzindikira malembo ndi maliwu ake**

1. Pezani malembo omwe akuphunzitsidwa mu Sitandade 1 ndi 2.
2. Kambiranani katchulidwe ka malembowa.
3. Sonyezani anzanu zomwe mwakambirana.
4. Perekani maganizo anu pa zomwe anzanu asonyeza.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Mulemberetu malembo onse pa tchati.
- Musonyeze ophunzira katchulidwe ka liwu lililonse.
- Muthandize ophunzira kutchula maliwu a malembowa moyenera.
- Muchite ntchitoyi mobwerezabwereza mpaka ophunzira atadziwa bwino katchulidwe ka maliwu a malembowa.

### Ntchito 4 Kukambirana zitsanzo za ntchito zophunzitsira nsanamira ya kuzindikira malembo ndi maliwu

1. Pezani zitsanzo za ntchito zophunzitsira nsanamira ya kuzindikira malembo ndi maliwu ake kuchokera m'buku la mphunzitsi ndi la ophunzira la Sitandade 1 ndi 2.
2. Kambiranani zitsanzo zomwe mwapeza.
3. Fotokozerani anzanu zomwe mwakambirana.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Mutsogolere ophunzira kupeza zitsanzo za ntchito zophunzitsira nsanamira ya kuzindikira malembo ndi maliwu ake.
- Musonyeze ophunzira kachitidwe ka ntchito (routine) iliyonse.
- Muombe mkota pa ntchitoyi.

### Ntchito 5 Kusonyeza kaphunzitsidwe ka kuzindikira malembo ndi maliwu ake mu Sitandade 1 ndi 2

1. Unikani ntchito zophunzitsira nsanamira ya kuzindikira malembo ndi maliwu ake.
2. Sonyezani momwe mungaphunzitsire ntchitozo.
3. Zukutani phunziro lililonse.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Muonetsetse kuti ophunzira akutsatira njira yoyamba ndi mphunzitsi, mphunzitsi ndi ophunzira, kenaka ophunzira paokha moyenera.
- Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.

### Ntchito 6 Kufotokoza nsanamira ya kuwerenga molondola, mofulumira ndi mosadodoma

1. Pezani ntchito zosiyanasiyana zomwe zingathandize ophunzira kuwerenga molondola, mofulumira ndi mosadodoma kuchokera m'mabuku a aphunzitsi a Sitandade 1 mpaka 4.
2. Kambiranani njira zomwe zingathandize ophunzira kuwerenga molondola, mofulumira ndi mosadodoma pa ntchito zomwe mwapeza.
3. Fotokozerani anzanu zomwe mwakambirana.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Mufufuziretu njira zomwe zingathandize ophunzira kuwerenga molondola, mofulumira ndi mosadodoma.
- Musonyeze ophunzira kachitidwe ka njira iliyonse.
- Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.

**Ntchito 7 Kusonyeza kaphunzitsidwe ka kuwerenga molondola, mofulumira ndi mosadodoma m'Sitandade 1 mpaka 4**

1. Unikani njira zophunzitsira nsanamira ya kuwerenga molondola, mofulumira ndi mosadodoma.
2. Sonyezani momwe mungaphunzitsire kuwerenga molondola, mofulumira ndi mosadodoma.
3. Zukutani phunziro lililonse.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Muonetsetse kuti ophunzira akutsatira njira yoyamba ndi mphunzitsi, mphunzitsi ndi ophunzira, kenaka ophunzira paokha moyenera.
- Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.

## Kufotokoza mwachidule

M'mutu uno, mwaphunzira nsanamira zisanu za kuwerenga. Mwasonyeza momwe mungaphunzitsire kuwerenga potsatira nsanamira zitatu izi: kumva ndi kutchula maliwu, kuzindikira malembo ndi maliwu ake, kuwerenga molondola, mofulumira ndi mosadodoma. Pomaliza, mwazukuta maphunziro omwe mwasonyeza.

### Kudziunika ndi kudziyesa

1. Fotokozani nsanamira zisanu za kuwerenga.
2. Fotokozani njira zosiyanasiyana zothandiza ophunzira kuwerenga molondola, mofulumira ndi mosadodoma.

## Matanthauzo a mawu

**Liwu** chimene chimamveka m'khutu poimba nyimbo, ng'oma, beru ndi zina

## Mabuku


Adams, MJ (1994). *Beginning to read: thinking and learning about print*. First Edition. England: The MIT Press.

Caldwell, JS (2014). *Reading assessment: a primer for teachers in the core era*.Third Edition. New York: The Guilford Press.

Centre for Language Studies (2000). *Mtanthauzira mawu wa Chinyanja. Blantyre:* Dzuka.

Cunningham, PM and Allington, RL (2011). *Classrooms that work: they can all read and write*. Fifth Edition. Boston: Pearson.

Malawi Institute of Education (2008). Maphunziro a m'sukulu za uphunzitsi m'Malawi: Chichewa buku la mphunzitsi, Domasi: MIE.

Malawi Institute of Education (2008). *Initial primary teacher education (IPTE): English tutor's handbook*. Domasi: MIE.

Malawi Institute of Education, (2009). Initial Primary Teacher Education (IPTE) through Open and Distance Learning (ODL): Chichewa Module 1. First Edition. Lilongwe: MIE Domasi

Vacca, RT etal (2014). *Content Area reading: literacy and learning across the curriculum*. 11th Edition. Upper Saddle River – NJ: Pearson Education, Inc.

*Student teacher's handbook 2*

## Kuwerenga koonjezera

https://www.readnaturally.com/research/5-components-of-reading
http://www.scsk12.org/scs/subjectareas/kweb/images/nationalreadingpanel_faq.pdf
https://cehdvision2020.umn.edu/blog/helping-kids-with-reading/

# MUTU 5 Kaphunzitsidwe ka kuwerenga (kupitiriza)

**Luso:** Kuwerenga
**Nthawi:** Maola 7
**Chigawo:** Choyamba

## Chiyambi

Kuwerenga ndi limodzi mwa maluso ofunika kwambiri m'phunziro la Chichewa. Mphunzitsi ayenera kudziwa momwe ayenera kuphunzitsira lusoli kuti athe kuphunzitsa moyenera. M'mutu 4 munaphunzira za luso la kuwerenga. M'mutuwo munaphunzira momwe mungaphunzitsire kuwerenga m'sukulu zapulayimale potsatira zina mwa nsanamira zisanu zophunzitsira kuwerenga.

M'mutu uno, mupitiriza kuphunzira nsanamira ya kudziwa mawu ndi matanthauzo ake ndi ya kumvetsa nkhani.

## Zizindikiro za kakhozedwe

Pakutha pa mutu uno, ophunzira:

- afotokoza nsanamira ya kudziwa mawu ndi matanthauzo ake.
- asonyeza kaphunzitsidwe ka nsanamira ya kudziwa mawu ndi matanthauzo ake.
- afotokoza nsanamira ya kumvetsa nkhani.
- asonyeza kaphunzitsidwe ka nsanamira ya kumvetsa nkhani.

## Mawu otsogolera

Kuphunzitsa kuwerenga pogwiritsa ntchito nsanamira zisanu za kuwerenga kumathandiza ophunzira kuzamitsa luso la kuwerenga. Mphunzitsi ayenera kudziwa ndi kumvetsa bwino nsanamirazi.

**Ntchito 1 Kufotokoza nsanamira ya kudziwa mawu ndi matanthauzo ake**

1. Kambiranani njira zothandiza ophunzira kupeza matanthauzo a mawu atsopano.
2. Fotokozerani anzanu zomwe mwakambirana
3. Pezani njira zosiyanasiyana zomwe zingathandize ophunzira kudziwa mawu ndi matanthauzo ake kuchokera m'mabuku a aphunzitsi a Sitandade 1 mpaka 4.
4. Fotokozerani anzanu zomwe mwapeza.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Mufufuziretu njira zomwe zingathandize ophunzira kupeza mawu atsopano ndi matanthauzo ake.
- Musonyeze ophunzira kachitidwe ka njirazi.
- Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.

**Ntchito 2 Kusonyeza kaphunzitsidwe ka kupeza matanthauzo a mawu m'Sitandade 1 mpaka 4**

1 Unikani njira zophunzitsira nsanamira ya kupeza matanthauzo a mawu.
2 Sonyezani momwe mungaphunzitsire ophunzira kupeza matanthauzo a mawu pogwiritsa ntchito njirazi.
3 Zukutani phunziro lililonse.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Muonetsetse kuti ophunzira akutsatira njira yoyamba ndi mphunzitsi, mphunzitsi ndi ophunzira, kenaka ophunzira paokha moyenera.
- Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.

**Ntchito 3 Kufotokoza nsanamira ya kumvetsa nkhani**

1 Kambiranani kaphunzitsidwe ka kumvetsa nkhani m'sitandade 1 mpaka 4.
2 Pezani ntchito za kumvetsa nkhani kuchokera m'mabuku a aphunzitsi a Sitandade 1 mpaka 4.
3 Kambiranani kusiyana kwa ntchito za kumvetsera nkhani ndi kumvetsa nkhani yomwe ophunzira awerenga.
4 Fotokozerani anzanu zomwe mwapeza.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Mutsogolere ophunzira kusiyanitsa ntchito za kumvetsera nkhani ndi kumvetsa nkhani zomwe ophunzira awerenga.
- Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.

**Ntchito 4 Kusonyeza kaphunzitsidwe ka kumvetsa nkhani m'Sitandade 1 mpaka 4**

1 Kambiranani njira zophunzitsira kumvetsa nkhani m'Sitandade 1 mpaka 4.
2 Pezani njirazi m'mabuku a aphunzitsi a Sitandade 1 mpaka 4.
3 Fotokozerani anzanu zomwe mwapeza.
4 Unikani njira zophunzitsira nsanamira ya kumvetsa nkhani.
5 Sonyezani momwe mungaphunzitsire kumvetsa nkhani pogwiritsa ntchito njirazi.
6 Zukutani phunziro lililonse.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Mufufuziretu njira zophunzitsira kumvetsa nkhani mu Sitandade 1 mpaka 4.
- Musonyeze ophunzira kachitidwe ka njirazi.
- Muonetsetse kuti ophunzira akutsatira njira yoyamba ndi mphunzitsi, mphunzitsi ndi

**Ntchito 5: Kuonerera phunziro la kuwerenga pogwiritsa ntchito nsanamira za kuwerenga mu Sitandade 1 mpaka 4**

1. Kambiranani mfundo zoyenera kutsatira poonerera phunziro la kuwerenga m'makalasi a Sitandade 1 mpaka 4.
   - Kodi mphunzitsi akutsatira dongosolo loyenera loyamba ndi mphunzitsi, mphunzitsi ndi ophunzira kenako ophunzira paokha?
   - Kodi mphunzitsi akutsatira dongosolo loonetsetsa kuti ophunzira akumvetsa zomwe akuphunzira?
   - Ndi nsanamira ziti zimene zaphunzitsidwa?
   - Phunziro latenga nthawi yochuluka bwanji?
   - Lembani zina zomwe mwaona.
2. Onererani phunziro la kuwerenga pogwiritsa ntchito mfundo zomwe mwakambirana.
3. Kambiranani zomwe mwaona.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Onetsetsani kuti ophunzira akudziwa zoyenera kuchita poonerera phunziro.
- Limbikitsani ophunzira kulemba zomwe akuona.

**Ntchito 6: Kusonyeza kaphunzitsidwe ka phunziro la kuwerenga potsatira nsanamira za kuwerenga**

1. Kambiranani m'magulu momwe mungaphunzitsire phunziro la kuwerenga mu Sitandade 1 mpaka 4.
2. Sonyezani momwe mungaphunzitsire phunziro lomwe mwakonza.
3. Kambiranani momwe phunziro layendera.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Mufufuziretu njira zophunzitsira kumvetsa nkhani m'Sitandade 1 mpaka 4.
- Musonyeze ophunzira kachitidwe ka njirazi.
- Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.
- Muonetsetse kuti ophunzira akutsatira njira yoyamba ndi mphunzitsi, mphunzitsi ndi ophunzira, kenaka ophunzira paokha moyenera.

## Kufotokoza mwachidule

M'mutu uno mwaphunzira nsanamira ziwiri za kuwerenga. Mwafotokoza za kudziwa mawu ndi matanthauzo ake ndi kumvetsa nkhani. Kenaka, mwasonyeza momwe mungaphunzitsire kuwerenga pogwiritsa ntchito nsanamirazi.

Potsiriza, mwaonerera ndi kuzukuta maphunziro a kuwerenga.

## Kudziunika ndi kudziyesa

1. Fotokozani njira zosiyanasiyana zothandiza ophunzira kupeza matanthauzo a mawu atsopano.
2. Pa maphunziro omwe munaonerera, ndi zinthu ziti zomwe sizinayende bwino?

### Mabuku


Adams, M.J. (1994). *Beginning to read: thinking and learning about print*. First Edition. England: The MIT Press.

Caldwell, JS (2014). *Reading Assessment: a primer for teachers in the core era*.Third Edition. New York: The Guilford Press.

Centre for Language Studies (2000). *Mtanthauzira mawu wa Chinyanja. Blantyre: Dzuka*.

Cunningham, PM and Allington, RL (2011). *Classrooms that work: they can all read and write*. Fifth Edition. Boston: Pearson.

Malawi Institute of Education (2008). *Chichewa buku la Mphunzitsi*. Domasi: MIE.

Malawi Institute of Education (2008).*Initial primary teacher education (IPTE): English tutor's handbook*, Domasi: MIE.

Ministry of Education, Science and Technology (2009). *Initial Primary Teacher Education through Open and Distance Learning* (ODL): Chichewa *Module 1*. First Edition. Lilongwe: DTED.

Vacca, RT etal (2014). C*ontent area reading: Literacy and learning across the curriculum*. 11th Edition. Upper Saddle River – NJ: Pearson Education, Inc.


## Kuwerenga koonjezera

https://www.readnaturally.com/research/5-components-of-reading

http://www.scsk12.org/scs/subjectareas/kweb/images/nationalreadingpanel_faq.pdf

https://cehdvision2020.umn.edu/blog/helping-kids-with-reading/

# MUTU 6 Kaphunzitsidwe ka kukonzekera kulemba

**Luso** : Kulemba
**Nthawi**: Maola 4
**Chigawo**: Choyamba

## Chiyambi

Mphunzitsi ayenera kuchita ntchito zosiyanasiyana m'phunziro la konzekera kulemba. Izi zimathandiza ophunzira kuti aphunzire kulemba mosavuta. Choncho mphunzitsi ayenera kutsatira ndondomeko ya phunziro la kulemba moyenera.

M'mutu uno, muphunzira ntchito zomwe mphunzitsi angachite ndi ophunzira pa phunziro la kukonzekera kulemba. Mufotokoza kufunika kwa zitchetche. Kenaka, mulemba ndondomeko yophunzitsira phunziro la kukonzekera kulemba. Pomaliza musonyeza momwe mungaphunzitsire kukonzekera kulemba.

## Zizindikiro za kakhozedwe

Pakutha pa mutu uno, ophunzira:

- afotokoza ntchito zomwe mphunzitsi angachite ndi ophunzira pa phunziro la kukonzekera kulemba.
- asonyeza kaphunzitsidwe ka kukonzekera kulemba.

## Mawu otsogolera

Pali ntchito zosiyanasiyana zomwe mphunzitsi angachite ndi ophunzira m'phunziro la kukonzekera kulemba. Pamene mphunzitsi akuphunzitsa phunziro la kukonzekera kulemba akuyenera kutsatira ndondomeko zomwe zimathandiza ophunzira kukhala ndi chidwi ndi phunziro. Imodzi mwa ntchito zomwe mphunzitsi angachite ndi ophunzira ndi kulemba zitchetche. Zitchetchezi zimalembedwa mosiyanasiyana motere:

***Kwera tsika kwera tsika***

Chitchetche chothandiza polemba malembo awa: A, M, N, W, X, V ndi Y monga:



***Tsika zungulira kwera***

Chitchetche chothandiza polemba malembo awa: o, u, a, b, c, e, g, l ndi t monga:



***Kwera zungulira tsika***

Chitchetche chothandiza polemba malembo awa: c, o, m, n ndi a monga:




***Kwera potoloza tsika***

Chitchetche chothandiza polemba malembo awa: s, f ndi g.




***Ima gona***

Chitchetche chothandiza polemba malembo awa: E, F, G, I, K, L ndi T monga:



*Pendeka pingasa*

Chitchetche chothandiza polemba malembo awa: Ww, K k, Vv ndi Yy monga:



**Ntchito 1 Kufotokoza ntchito zomwe mphunzitsi angachite ndi ophunzira pa phunziro la kukonzekera kulemba**

1 Kambiranani ntchito zomwe mphunzitsi angachite ndi ophunzira pa phunziro la kukonzekera kulemba.
2 Lembani zomwe mwakambirana.
3 Fotokozerani anzanu zomwe mwalemba.

**Malangizo kwa mphunzitsi**
Mufufuziretu ntchito zomwe mphunzitsiangachite ndi ophunzira pa phunziro la kukonzekera kulemba.

**Ntchito 2 Kufotokoza kufunika kwa zitchetche**

1 Unikani zitchetche zosiyanasiyana.
2 Lembani zitchetche zosiyanasiyana.
3 Sonyezani anzanu zomwe mwalemba.
4 Kambiranani kufunika kwa zitchetche.
5 Lembani zomwe mwakambirana.
6 Fotokozerani anzanu zomwe mwalemba.

**Malangizo kwa mphunzitsi**
- Mulemberetu mfundo zosonyeza kufunika kwa zitchetche.
- Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.

**Ntchito 3 Kulemba ndondomeko yophunzitsira phunziro la kukonzekera kulemba**

1 Unikani ntchito zomwe mphunzitsi angachite ndi ophunzira pa phunziro la kukonzekera kulemba.
2 Kambiranani ndondomeko yophunzitsira phunziro la kukonzekera kulemba.
3 Lembani ndondomeko yophunzitsira phunziro la kukonzekera kulemba.
4 Fotokozerani anzanu zomwe mwakambirana.

**Malangizo kwa mphunzitsi**
- Mulemberetu ndondomeko yophunzitsira phunziro la kukonzekera kulemba.
- Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.

**Ntchito 4 Kuonerera phunzilo la kukonzekera kulemba**

1. Kambiranani mfundo zoyenera kutsatira poonerera phunziro la kukonzekera kulemba mu Sitandade 1 ndi 2 motere:
   - Kodi mphunzitsi akutsatira dongosolo loyenera loyamba ndi mphunzitsi, mphunzitsi ndi ophunzira, kenaka ophunzira paokha?
   - Kodi mphunzitsi akutsatira dongosolo loonetsetsa kuti ophunzira akumvetsa zomwe akuphunzira?
   - Kodi ophunzira akupatsidwa mpata wokwanira woyesera kulemba?
   - Phunziro latenga nthawi yochuluka bwanji?
   - Lembani zina zomwe mwaona.
2. Onererani phunziro la kukonzekera kulemba.
3. Kambiranani zomwe mwaona.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Onetsetsani kuti ophunzira akudziwa zoyenera kuchita.
- Limbikitsani ophunzira kulemba zomwe akuona.
- Onetsetsani kuti mwabweretsa mabuku ophunzitsira Chichewa mu Sitandade 1 mpaka 4.
- Perekani nthawi yokwanira kuti ophunzira akonzekere phunziro lophunzitsa kuwerenga.

**Ntchito 5 Kusonyeza kaphunzitsidwe ka kukonzekera kulemba**

1 Unikani ndondomeko yophunzitsira phunziro la kukonzekera kulemba yomwe munalemba.

2 Sonyezani momwe mungaphunzitsire kukonzekera kulemba mu Sitandade 1.

3 Perekani maganizo anu pa ntchito yomwe anzanu achita.

**Malangizo kwa mphunzitsi**
Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.

## Kufotokoza mwachidule

M'mutu uno mwaphunzira zomwe mphunzitsi angachite ndi ophunzira pa phunziro la kukonzekera kulemba. Mwafotokoza kufunika kwa zitchetche. Pomaliza, mwaphunzitsa, mwaonera ndi kuzukuta phunziro la kukonzekera kulemba.

## Kudziunika ndi kudziyesa

1 Fotokozani ntchito zitatu zomwe mungachite ndi ophunzira pa phunziro la kukonzekera kulemba.

2 Fotokozani zitsanzo ziwiri za zitchetche.

3 Yerekezani kuti mphunzitsi wa Sitandade 1 amanyozera kuphunzitsa phunziro la kukonzekera kulemba pogwiritsa ntchito zitchetche. Kodi mungamulangize zotani?

## Matanthauzo a mawu

**Zitchetche:** mapatani osiyanasiyana omwe amathandiza ophunzira kulemba malembo

## Mabuku

Malawi Institute of Education (2008). *Maphunziro a m'sukulu zauphunzitsi m'Malawi buku la mphunzitsi*. Domasi: MIE.

## Kuwerenga koonjezera

Unduna wa za maphunziro (1998). *Student teachers handbook 2* (Revised draft version). Domasi: MIE.

# MUTU 7 Kaphunzitsidwe ka mitundu ya kulemba

**Luso:** Kulemba
**Nthawi:** Maola 1
**Chigawo:** Choyamba

## Chiyambi

Kulemba ndi luso limene munthu aliyense ayenera kulidziwa. Luso la kulemba limathandiza ophunzira kudziwa kulemba nkhani zochitika ndi zopeka m'njira zosiyanasiyana.

M'mutu uno, muphunzira mitudu iwiri ya kulemba. Kenaka musonyeza momwe mungaphunzitsire mitundu iwiriyi.

## Zizindikiro zakakhozedwe

Pakutha pa mutu uno, ophunzira asonyeza kaphunzitsidwe ka mitundu ya kulemba.

## Mawu otsogolera

Luso la kulemba ndi lofunika mu njira zosiyanasiyana. Choncho n'kofunika kuti mphunzitsi aphunzitse moyenera ndi cholinga chokulitsa lusoli mwa ophunzira. Pali mitundu iwiri ya kulemba yotsatirayi:

**Kulemba kosalumikiza**
Uku ndi kulemba kwachimodzichimodzi kapena kosindikiza monga:

Ana akusesa.

**Kulemba kolumikiza/kwachikhukhudza/ moguza**

Iwo amaphunzira Chichewa.

Kulemba kwachikhukhudza kulipo kwa mitundu iwiri.

**Kulemba kwachipama**
Kulemba kotereku adayambitsa ndi Austin Palmer wa ku America. Kulemba kwachipama kumakhala ndi timichira ndi makaka ambiri monga:

Buku la mphunzitsi

**Kulemba kwa chimariyoni**
Kulemba kotereku adayambitsa ndi Mngerezi wotchedwa Marion Richardson. Malembo a kulemba kwa chimariyoni amaweramira chakutsogolo pang'ono komanso amagonera mbali imodzi monga:

Mango ndi chipatso chabwino.

**Ntchito 1 Kufotokoza mitundu ya kulemba**

1. Kambiranani tanthauzo la kulemba.
2. Kambiranani mitundu ya kulemba.
3. Fotokozerani anzanu zomwe mwakambirana.

**Malangizo kwa mphunzitsi**
Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.

**Ntchito 2 Kulemba ziganizo potsatira mitundu ya kulemba**

1 Unikani mitundu iwiri ya kulemba.
2 Lembani ziganizo potsatira mitundu iwiri ya kulemba.
3 Sonyezani anzanu zomwe mwalemba.
4 Perekani maganizo anu pa ntchito yomwe anzanu achita.

**Malangizo kwa mphunzitsi**
Muonetsetse kuti muli ndi zitsanzo za mitundu ya kulemba.

**Ntchito 3 Kusonyeza kaphunzitsidwe ka mitundu ya kulemba**

1 Konzekerani phunziro la mitundu ya kulemba.
2 Sonyezani momwe mungaphunzitsire mitundu ya kulemba mu Sitandade 3.
3 Zukutani maphunziro a anzanu.

**Malangizo kwa mphunzitsi**
Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.

## Kufotokoza mwachidule

M'muto uno, mwaphunzira kufunika kwa kulemba. Mwaphunzira mitundu yakulemba. Kenaka, mwasonyeza momwe mungaphunzitsire phunziro la mitundu ya kulemba.

## Kudziunika ndi kudziyesa

1 Fotokozani kufunika kwa kulemba.
2 Fotokozani mitundu iwiri ya kulemba.
3 Perekani maganizo anu pa mitundu iwiri ya kulemba.

## Matanthauzo a mawu

**Kulemba**: Kusindikiza malembo moyenera kuti aoneke bwino ndicholinga chopereka tanthauzo lomveka bwino.

## Mabuku

Malawi Institute of Education (2008). *Maphunziro a msukulu zauphunzitsi m'Malawi buku lamphunzitsi*. Domasi: MIE

Unduna wa za maphunziro (1998). *Student teachers handbook 2* (Revised draft version). Domasi: MIE.

# MUTU 8 Kulemba dongosolo la ntchito

**Luso**: Kulemba
**Nthawi**: Maola 3
**Chigawo**: Choyamba

## Chiyambi

Ophunzira uphunzitsi ayenera kuphunzira kalembedwe ka dongosolo la ntchito chifukwa luso la kuphunzitsa lagona pa kukonzekera ntchito yokaphunzitsa. Dongosolo la ntchito limaonetsa mwatsatanetsatane ntchito zoyenera kukaphunzitsa ophunzira.

M'mutu uno, muphunzira zifukwa zolembera dongosolo la ntchito. Muphunzira zofunika kuganizira polemba dongosolo la ntchito komanso mufotokoza kalembedwe kake. Potsiriza mulemba dongosolo la ntchito.

## Zizindikiro za kakhozedwe

Pakutha pa mutu uno, ophunzira alemba dongosolo la ntchito.

## Mawu otsogolera

Munthu pofuna kupambana pa zochitika za tsiku ndi tsiku ayenera kulemba ndondomeko ya zomwe akufuna kuchita. Choncho n'kofunika kuti mphunzitsi azikonzeratu ntchito yokaphunzitsa. Mphunzitsi amene salemberatu dongosolo la ntchito amalephera kuphunzitsa bwino. Ndi bwino kuti mphunzitsi azindikire momwe angalembere dongosolo la ntchito. Akuyeneranso kudziwa magawo a dongosolo la ntchito ndi zomwe angalembe m'gawo lililonse. Magawo a dongosolo la ntchito alipo asanu ndi limodzi. Magawowa ndi awa:

***Sabata ndi masiku***
Mu gawo ili mphunzitsi amalemba sabata ndi masiku omwe aphunzitse ntchito yomwe wakonza.

***Zizindikiro za kakhozedwe***
Izi ndi zomwe ophunzira achite posonyeza kuti amvetsa zomwe aphunzira.

***Ntchito yokaphunzitsa***
Uwu ndi mndandanda wa mitu ya ntchito yomwe mphunzitsi amakonza kuti akaphunzitse pa sabata iliyonse.

***Njira zophunzitsira, zophunzirira ndi zoyesera***

Izi ndi njira zomwe mphunzitsi amagwiritsa ntchito pophunzitsa mitu yomwe wakonza.

***Zipangizo zophunzitsira, zophunzirira ndi zoyesera***
Izi ndi zinthu zonse zimene mphunzitsi ndi ophunzira agwiritse ntchito pa mitu yomwe mphunzitsi wakonza.

***Mabuku***
Awa ndi mabuku omwe mphunzitsi ndi ophunzira angagwiritse ntchito pophunzitsa ndi kuphunzira ntchito yomwe mphunzitsi wakonza.

**Chitsanzo cha dongosolo la ntchito**

Chitsanzo cha dongosolo la ntchito ya
Sitandade 3

| Sabata ndi masiku | Zizindikiro za kakhozedwe | Ntchito yokaphunzitsa | Njira zophunzitsira, zophunzirira ndi zoyesera | Zipangizo zophunzitsira, zophunzirira ndi zoyesera | Mabuku | Zomwe ophunzira akuchita | Ndamanga |
|---|---|---|---|---|---|---|---|
| 1<br><br>10 May, 2017<br><br>mpaka<br><br>14 May, 2017 | Ophunzira:<br>• amva katchulidwe ka /**nd**/<br>• awerenga maphatikizo ndi mawu okhala ndi /**nd**/<br><br>• alosera nkhani | **Mutu 2:**<br>**Phunziro 1 ndi 2**:<br>• kuzindikira liwu la /**nd**/<br>• kuwerenga maphatikizo ndi mawu okhala ndi /nd/<br><br>**Phunziro 3 ndi 4:**<br>• kulosera ndi kuwerenga | Kufunsa ndi kuyankha mafunso<br><br>Ntchito ya awiriawiri | Zithunzi<br><br>Makadi a mawu<br><br>Makadi a maphatikizo<br><br>Mtengo wa mawu<br><br>Mabuku oonjezera | Malawi Institute of Education. (2017) Chichewa buku la mphunzitsi la Sitandade 2. Domasi : M.I.E Tsamba … mpaka…<br><br>Malawi Institute of Education. | | |

| | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | • awerenga nkhani mofulumira<br><br>• atsiriza mawu<br>• amvetsera nthano<br>• atchula /**ch**/<br>• alemba mawu okhala ndi **ch**<br>• apanga mawu okhala ndi **ch**<br><br>• awerenga nkhani<br><br>• apereka matanthauzo | nkhani<br>• kuwerenga nkhani mofulumira<br><br>**Phunziro 5 ndi 6:**<br>• Kutsiriza mawu<br>• Kumvetsera nthano<br>• Kutchula liwu la /**ch**/<br>• Kulemba mawu okhala ndi **ch**<br>• Kupanga mawu okhala ndi **ch**<br><br>**Phunziro 7 ndi 8**:<br>• Kuwerenga nkhani | Ntchito ya m'magulu<br><br>Ntchito ya mmodzimmod zi<br><br>Kusonyeza | | (2017). Chichewa buku la Ophunzira la Sitandade 2. Domasi : M.I.E Tsamba… mpaka… | | |

| | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | a mawu<br><br>• awerega mabuku oonjezera<br>• asonyeza ntchito yomwe achita m'sabatayi<br>• abwereza ntchito yomwe sanachite bwino m'sabatayi | • Kupereka matanthauzo a mawu<br>• Kulemba mawu (Ntchito B)<br><br>**Phunziro 9 ndi 10**:<br>• Kuwerenga mabuku oonjezera ndi kuyesa ophunzira<br><br>• Kubwereza ntchito ya m'sabatayi | | | | | |

**Ntchito 1 Kufotokoza zifukwa zolembera dongosolo la ntchito**

1 Kambiranani zifukwa zolembera dongosolo la ntchito.
2 Kambiranani zofunika kuganizira polemba dongosolo la ntchito.
3 Lembani zomwe mwakambirana.
4 Fotokozerani anzanu zomwe mwalemba.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Mufufuziretu mfundo zosonyeza kufunika kolemba dongosolo la ntchito.
- Mufufuziretu zofunika kuganizira polemba dongosolo la ntchito.

**Ntchito 2 Kufotokoza kalembedwe ka dongosolo la ntchito**

1 Kambiranani kalembedwe ka dongosolo la ntchito.
2 Lembani zomwe mwakambirana.
3 Fotokozerani anzanu zomwe mwalemba.

**Malangizo kwa mphunzitsi**
Mulemberetu chitsanzo cha dongosolo la ntchito.

**Ntchito 3 Kulemba dongosolo la ntchito**

1 Unikani chitsanzo cha dongosolo la ntchito.
2 Unikani mabuku a mphunzitsi ndi a ophunzira a Sitandade 1 mpaka 8 kuti muone ntchito yoyenera kulemba mu dongosolo la ntchito.
3 Lembani dongosolo la ntchito.
4 Sonyezani anzanu zomwe mwalemba.
5 Perekani maganizo anu pa ntchito yomwe anzanu achita.

**Malangizo kwa mphunzitsi**
Mulemberetu chitsanzo cha dongosolo la ntchito.

## Kufotokoza mwachidule

M'mutu uno, mwaphunzira zifukwa zolembera dongosolo la ntchito. Mwaphunzira zofunika kuganizira polemba dongosolo la ntchito. Kenaka mwafotokoza kalembedwe ka dongosolo la ntchito. Potsiriza mwalemba ndi kuzukuta dongosolo la ntchito.

## Kudziunika ndi kudziyesa

1 Fotokozani kufunika kwa magawo a zizindikiro za kakhozedwe ndi mabuku mu dongosolo la ntchito.
2 Ndi ubwino wanji umene ungapezeke polemberatu dongosolo la ntchito?

## Matanthauzo a mawu

**Dongosolo la ntchito** mndandanda wa ntchito yomwe mphunzitsi amakonza pa mitu yochokera mu silabasi yokaphunzitsira yokwanira chigawo chimodzi kapena chaka chonse cha sukulu.

## Mabuku

Malawi Institute of Education (2008). *Maphunziro a m'sukulu zauphunzitsi m'Malawi buku la Mphunzitsi*. Domasi: MIE

Unduna wa za maphunziro (1998). *Student teachers handbook 1* (Revised draft version). Domasi: MIE.

Mtunda, FG et al (1997). *An intoduction to the theory and practice of teaching*. Blantyre: Dzuka Publishing Company Limited.

# MUTU 9 Kulemba chikonzekero cha phunziro

**Luso** : Kulemba
**Nthawi** Maola 3
**Chigawo**: Choyamba

## Chiyambi

Mphunzitsi akuyenera kulemba chikonzekero cha phunziro lililonse. Choncho ndi kofunika kuti mphunzitsi azindikire momwe angalembere chikonzekero cha phunziro.

M'mutu uno, muphunzira kalembedwe ndi kagwiritsidwe ntchito ka chikonzekero cha phunziro.

### Zizindikiro za kakhozedwe

Pakutha pa mutu uno, ophunzira:

- afotokoza kufanana ndi kusiyana kwa chikonzekero cha phunziro cholemberatu cha mu Sitandade 1 mpaka 4 ndi chikonzero cha phunziro cha mu Sitandade 5 mpaka 8.
- asonyeza kagwiritsidwe ntchito ka chikonzekero cha phunziro cholemberatu.

### Mawu otsogolera

Chikonzekero cha phunziro chili ndi magawo asanu ndi limodzi. Magawowa ndi awa:

***Zoyambirira (Mayambiro)***
Zina mwa zomwe mphunzitsi amalemba mu gawo la zoyambirira kapena mayambiro ndi izi: kalasi, tsiku, nthawi, phunziro, luso ndi mutu womwe akukonzekera kukaphunzitsa.

***Zizindikiro za kakhozedwe***
Zizindikiro za kakhozedwe zimasonyeza zomwe ophunzira achite m'kalasi. N'kofunika kulemba zizindikiro momveka bwino. Ziyenera kukhala ndi aneni osonyeza kugwira ntchito, mawu osonyeza momwe ophunzira achitire komanso kuonetsetsa kuti mu chizindikiro chimodzi musakhale aneni awiri.

***Zipangizo zophunzitsira, zophunzirira ndi zoyesera***
Mu gawoli mphunzitsi amasonyezamo zipangizo zonse zimene agwiritse ntchito pophunzitsa. Zimathandizanso kuunikira ngati ophunzira atsatira bwino phunzirolo kapena ayi.

***Chiyambi cha phunziro***
Chiyambi cha phunziro ndi chofunika kwambiri chifukwa chimapereka chithunzithunzi cha zomwe ophunzira akuyembekezera kuphunzira mu phunziro limenelo. Chiyambi chiyenera kukhala chomveka bwino, chokondweretsa, chopatsa chidwi komanso chogwirizana ndi phunziro.

***Ndondomeko***
Ili ndi gawo lomwe mphunzitsi amalembamo magawo a phunziro.

Magawowo ndi ntchito ndi njira yophunzitsira ntchitoyo. Polemba ndondomeko, n'kofunika kuonetsetsa kuti mphunzitsi watsata zizindikiro za kakhozedwe, wayala bwino lomwe mfundo mu gawo lililonse komanso kuti mfundozo zagwirizana bwino n'cholinga chothandiza ophunzira kuti amvetse phunzirolo.

*Mathero*

Ili ndi gawo lomwe limathandiza mphunzitsi kudziwa ngati ophunzira ake amvetsa bwino phunziro lomwe amaphunzitsa. Zomwe zimachitika m'gawoli ndi monga kubwereza ntchito mwachidule, kufunsa ophunzira kuti afotokoze zomwe aphunzira kapena kuyankha mafunso, kuchita sewero, kulemba mawu kapena ziganizo, kulakatula ndakatulo ndi kuimba nyimbo.

**Ntchito 1 Kufotokoza zifukwa zolembera chikonzekero cha phunziro**

1 Kambiranani zifukwa zolembera chikonzekero cha phunziro.
2 Lembani zomwe mwakambirana.
3 Fotokozerani anzanu zomwe mwalemba.

**Malangizo kwa mphunzitsi**
Mufufuziretu zifukwa zolembera chikonzekero cha phunziro.

**Ntchito 2 Kulemba chikonzekero cha phunziro cha mu Sitandade 5 mpaka 8**

1 Kambiranani kalembedwe ka chikonzekero cha phunziro.
2 Lembani chikonzekero cha phunziro chomwe mwakambirana pogwiritsa ntchito mabuku a aphunzitsi ndi a ophunzira a Sitandade 5 mpaka 8.
3 Sonyezani anzanu zomwe mwalemba.

**Malangizo kwa mphunzitsi**
- Mulemberetu chitsanzo cha chikonzekero cha phunziro cha mu Sitandade 5 mpaka 8.
- Mutsogolere ophunzira kulemba chikonzekero cha phunzirochi.

**Chitsanzo cha chikonzekero cha phunziro cha Sitandade 5 mpaka 8**

Kalasi: Sitandade 5
Tsiku: 10 September, 2017
Phunziro: Chichewa
Nthawi: 8:00 mpaka 8:30 m'mawa
Mutu1: Phunziro 4

**Zizindikiro za kakhozedwe**

Ophunzira:
- apatsana moni.
- ayankha moni molondola.
- …………………………………
- …………………………………
- …………………………………

**Zipangizo zophunzitsira, zophunzirira ndi zoyesera**
- Chithunzi cha anthu akupatsana moni

- Chithunzi cha anthu akutsanzikana
- ……………………………………

| Zochita mphunzitsi | Zochita ophunzira |
|---|---|
| **Chiyambi**<br>Uzani ophunzira kuti afotokoze zomwe anthu amachita popatsana moni. | Kufotokoza zomwe anthu amachita popatsana moni. |
| **Ndondomeko**<br>Gawo 1<br>…………………<br>…………………<br>……….. | ……………………<br>……………………<br>……. |
| Gawo 2<br>…………………<br>…………………<br>……… | ……………………<br>……………………<br>…….. |
| Gawo 3<br>…………………<br>…………………<br>……… | ……………………<br>……………………<br>…….. |
| Mathero<br>…………………<br>…………………<br>……….. | ……………………<br>……………………<br>…….. |

**Ndamanga:**

| Zomwe zayenda bwino | Zomwe sizinayende bwino | Zoyenera kuchita |
|---|---|---|
| | | |

**Ntchito 3 Kufotokoza kagwiritsidwe ntchito ka chikonzekero cha phunziro cholemberatu mu Sitandade 1 mpaka 4**

1. Unikani chikonzekero cha phunziro cholemberatu cha mu Sitandade 1 mpaka 4 (Scripted Lesson Plan) kuchokera mu buku la mphunzitsi.
2. Lembani mfundo zoyenera kutsatira pophunzitsa (Lesson notes).
3. Fotokozerani anzanu zomwe mwalemba.
4. Kambiranani kufunika kolemba mfundo zoyenera kutsatira pophunzitsa.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Mutsogolere ophunzira kulemba mfundo zoyenera kutsatira pophunzitsa.
- Mutsogolere ophunzira kuzindikira kufunika kolemba mfundo zoyenera kutsatira pophunzitsa.

**Chitsanzo cha mfundo zoyenera kutsatira pophunzitsa (Lesson notes).**

Kalasi: Sitandade 2
Tsiku: 10 September, 2017
Phunziro: Chichewa
Nthawi: 8:00 mpaka 8:30 m'mawa
Mutu: Mutu 1 phunziro 4

**Zizindikiro za kakhozedwe**

Ophunzira:

- apatsana moni.
- ayankha moni molondola.
- ………………………………… ………………………………

**Zipangizo zophunzitsira, zophunzirira ndi zoyesera**

- Chithunzi cha anthu akupatsana moni
- Chithunzi cha anthu akutsanzikana
- ………………………………… ……………………

**Chiyambi**

Imbani nyimbo iliyonse yogwirizana ndi phunziro.

**Ndondomeko**

Ntchito 1:

- ………………………………… Lembani zomwe muphunzitse ndi momwe musonyezere
- ………………………………… Lembani zomwe inu ndi ophunzira muchite ndi momwe muchitire.
- ………………………………… Lembani zomwe ophunzira achite paokha ndi momwe achitire.
- 

Ntchito 2:

- ………………………………… Lembani zomwe muphunzitse ndi momwe musonyezere
- ………………………………… Lembani zomwe inu ndi ophunzira muchite ndi momwe muchitire.
- ………………………………… Lembani zomwe ophunzira achite paokha ndi momwe achitire.

Ntchito 3:

- ………………………………… Lembani zomwe muphunzitse ndi momwe musonyezere.
- ………………………………… Lembani zomwe inu ndi ophunzira muchite ndi momwe muchitire.
- ………………………………… Lembani zomwe ophunzira achite paokha ndi momwe achitire.

**Mathero:**

Lembani mathero ogwirizana ndi phunziro.

**Ndamanga:**

| Zomwe zayenda bwino | Zomwe sizinayende bwino | Zoyenera kuchita |
|---|---|---|
| | | |

**Ntchito 4 Kufananitsa ndi kusiyanitsa chikonzekero cha phunziro cha mu Sitandade 5 mpaka 8 ndi chikonzekero cha phunziro cholemberatu cha mu Sitandade 1 mpaka 4.**

1. Fananitsani chikonzekero cha phunziro cha mu Sitandade 5 mpaka 8 ndi chikonzekero cha phunziro cholemberatu cha mu Sitandade 1 mpaka 4.
2. Siyanitsani chikonzekero cha phunziro cha m'Sitandade 5 mpaka 8 ndi chikonzekero cha phunziro cholemberatu cha mu Sitandade 1 mpaka 4.

3 Fananitsani zikonzekero ziwirizi ndi mfundo zoyenera kutsata pophunzitsa (Lesson notes) zomwe munalemba mu ntchito 3.
4 Fotokozerani anzanu zomwe mwapeza.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Mutsogolere ophunzira kufananitsa chikonzekero cha phunziro cha m'Sitandade 5 mpaka 8 ndi chikonzekero cha phunziro cholemberatu cha mu Sitandade 1 mpaka 4 komanso mfundo zoyenera kutsatira pophunzitsa zomwe ophunzira analemba mu ntchito 3.
- Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.

**Ntchito 5 Kusonyeza kagwiritsidwe ntchito ka chikonzekero cha phunziro cholemberatu**

1 Unikaninso chikonzekero cha phunziro cholemberatu.
2 Unikaninso mfundo zoyenera kutsatira pophunzitsa.
3 Sonyezani momwe mungagwiritsire ntchito chikonzekero cholemberatu pophunzitsa mu Sitandade 1 mpaka 4.
4 Perekani maganizo anu pa ntchito yomwe anzanu achita.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.

## Kufotokoza mwachidule

M'mutu uno mwaphunzira zifukwa zolembera chikonzekero cha phunziro ndipo mwalemba chikonzekero cha phunziro. Mwasonyeza momwe mungagwiritsire ntchito chikonzekero cha phunziro cholemberatu mu Sitandade 1 mpaka 4. Mwafananitsa ndi kusiyanitsa chikonzekero cha phunziro cholemberatu cha Sitandade 1 mpaka 4 ndi cha Sitandade 5 mpaka 8. Pomaliza, mwasonyeza momwe mungagwiritsire ntchito chikonzekero cha phunziro cholemberatu pophunzitsa mu Sitandade 1 mpaka 4.

## Kudziunika ndi kudziyesa

1 Fotokozani zomwe mungalembe m'magawo a chikonzekero cha phunziro.
2 Fotokozani ubwino ndi kuipa kwa chikonzekero cha phunziro cholemberatu.

## Matanthauzo a mawu

**Chikonzekero cha phunziro:** Dongosolo la ntchito imene mphunzitsi amalemba pokonzekera kukaphunzitsa mosadodoma pa tsiku lotsatira kuchokera mu dongosolo la ntchito lomwe adalemba kale.

### Mabuku

Malawi Institute of Education (2008). *Maphunziro a msukulu zauphunzitsi mMalawi buku la mphunzitsi*. Domasi: MIE

Unduna wa za maphunziro (1998). *Student teachers handbook 1* (Revised draft version). Domasi: MIE.

Mtunda, FG et al (1997). *An Intoduction to the theory and practice of teaching*. Blantyre: Dzuka.

Obanya, P (1980). *General methods of teaching*. London: Macmillan Education LTD.

# MUTU10 Kulemba zotsatira za ntchito yomwe ndaphunzitsa

**Luso:** Kulemba
**Nthawi:** Maola 1
**Chigawo:** Choyamba

## Chiyambi

Ophunzira ayenera kuphunzira kalembedwe ka zotsatira za ntchito yomwe ndaphunzitsa. Gawoli ndi lofunika chifukwa limasonyeza ntchito yomwe ophunzira achita ndi momwe ntchitoyo yayendera.

M'mutu uno, muphunzira kalembedwe ka zotsatira za ntchito yomwe ndaphunzitsa.

## Zizindikiro za kakhozedwe

Pakutha pa mutu uno, ophunzira alemba zotsatira za ntchito yomwe ndaphunzitsa.

## Mawu otsogolera

Gawo la zotsatira za ntchito yomwe ndaphunzitsa lili ndi magawo awiri omwe ndi: zomwe ophunzira akuchita ndi ndamanga. Mphunzitsi ayenera kudziwa kalembedwe ka zotsatira za ntchito yomwe ndaphunzitsa. Mphunzitsi akuyenera kulemba zotsatira za ntchito yomwe ndaphunzitsa kuti adziwe zomwe ophunzira amvetsa ndi zomwe sanamvetse. Zikaoneka kuti ophunzira sanamvetse, mphunzitsi amayenera kubwereza phunzirolo pogwiritsa ntchito njira zina zomuthandizira kuti phunzirolo limveke bwino. Izi zimathandiza mphunzitsi kupeza njira zoyenera kuti pamene akubwereza phunzirolo, ophunzira amvetse. Kulemba zotsatira za ntchito yomwe ndaphunzitsa kumathadizanso mphunzitsi kutsatira bwino mitu imene waphunzitsa kale.

### Ntchito 1 Kuunika dongosolo la ntchito ndi chikonzekero cha phunziro

1 Unikani dongosolo la ntchito lomwe mudalemba ndi chikonzekero cha phunziro chomwe mudagwiritsa nthito posonyeza kuphunzitsa.
2 Lembani mfundo kuchokera mu gawo la ndamanga la chikonzekero cha phunziro.
3 Fotokozerani anzanu zomwe mwalemba.

**Malangizo kwa mphunzitsi**
Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.

### Ntchito 2 Kulemba zotsatira za ntchito yomwe ndaphunzitsa

1 Kambiranani momwe mungalembere zomwe ophunzira akuchita ndi ndamanga.
2 Lembani zomwe ophunzira akuchita ndi ndamanga pogwiritsa ntchito dongosolo

la ntchito ndi chikonzekero cha phunziro.

3 Fotokozerani anzanu zomwe mwalemba.

4 Zukutani ntchito yomwe anzanu alemba.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Muonenetse kuti muli ndi chitsanzo cha zotsatira za ntchito yomwe ndaphunzitsa.
- Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.

## Kufotokoza mwachidule

M'mutu uno, mwaphunzira kulemba zotsatira za ntchito yomwe ndaphunzitsa. Kenaka, mwalemba ndi kuzukuta gawo la zotsatira za ntchito yomwe ndaphunzitsa.

## Kudziunika ndi kudziyesa

**1** Fotokozani zomwe mungalembe m'magawo a zotsatira za ntchito yomwe ndaphunzitsa.

**2** Pophunzitsa, mwazindikira kuti ophunzira ambiri sanamvetse phunziro, mungalembe zotani mu gawo la zotsatira za ntchito yomwe ndaphunzitsa?

## Matanthauzo a mawu

**Zotsatira za ntchito yomwe ndaphunzitsa**: Dongosolo lomwe limasonyeza ntchito yomwe ophunzira achita ndi momwe ntchitoyo yayendera mu sabata.

## Mabuku


Malawi Institute of Education (2008). *Maphunziro a m'sukulu zauphunzitsi m'Malawi Buku la mphunzitsi*. Domasi: MIE

Unduna wa za maphunziro (1998). *Student teachers handbook 1* (Revised draft version). Domasi: MIE.

Mtunda, FG et al (1997). *An Intoduction to the theory and practice of teaching*. Blantyre: Dzuka Publishing Company Limited.

Obanya, P (1980). *General methods of teaching*. London: Macmillan Education LTD.

# MUTU 11 Kaphunzitsidwe ka malamulo a chiyankhulo

**Luso:** Kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo

**Nthawi:** Maola 6

**Chigawo:** Choyamba:

## Chiyambi

Luso la kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo ndi lofunika kwambiri kwa ophunzira. Mphunzitsi akuyenera kuzindikira lusoli ndi cholinga choti athandize ophunzira moyenera.

M'mutu uno, muphunzira kusiyana kwa chiyankhulo cha Chichewa cham'madera. Muphunzira kufunika kwa kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo. Muphunziranso kugwiritsa ntchito mawu oyenera m'chiganizo. Muchita kafukufuku wa mitundu ya mawu. Kenaka, mufotokoza njira ndi ndondomeko zophunzitsira, zophunzirira ndi zoyesera kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo. Pomaliza, musonyeza momwe mungaphunzitsire phunziro la kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo.

## Zizindikiro zakakhozedwe

Pakutha pa mutu uno, ophunzira:

- afotokoza zomwe zimalepheretsa ophunzira kugwirita ntchito malamulo a chiyankhulo.
- agwiritsa ntchito mawu oyenera m'chiganizo.
- asonyeza kaphunzitsidwe ka phunziro la kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo

## Mawu otsogolera

Chiyankhulo chilichonse chimakhala ndi malamulo ake amene amagwiritsidwa ntchito poyankhula kapena polemba. Malamulowo ndi ofunika kwambiri chifukwa amathandizira kuti zoyankhula kapena zolemba zipereke tanthauzo lomveka bwino. Choncho ndi koyenera kuti mphunzitsi azindikire kuphunzitsa moyenera phunziro la kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo.

**Ntchito 1 Kufotokoza kusiyana kwa chiyankhulo cha Chichewa cha m'madera**

1 Kambiranani kusiyana kwa chiyankhulo cha Chichewa cham'madera.
2 Lembani zomwe mwakambirana.
3 Fotokozerani anzanu zomwe mwalemba.

**Malangizo kwa mphunzitsi**
Mufufuziretu zitsanzo zosonyeza kusiyana kwa Chichewa choyankhulidwa m'madera osiyanasiyana.

**Ntchito 2 Kufotokoza zomwe zimalepheretsa ophunzira kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo**

1. Kambiranani kufunika kwa malamulo a chiyankhulo.
2. Kambiranani zomwe zimalepheretsa ophunzira kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo.
3. Lembani zomwe mwakambirana.
4. Fotokozerani anzanu zomwe mwalemba.
5. Perekani maganizo anu pa zomwe anzanu afotokoza.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Mufufuziretu mfundo zosonyeza kufunika kwa malamulo a chiyankhulo.
- Mufufuziretu zomwe zimalepheretsa ophunzira kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo.

**Ntchito 3 Kugwiritsa ntchito mawu oyenera m'chiganizo**

**1** Konzani ziganizo zotsatirazi kuti zikhale m'Chichewa chomveka bwino.

a. Misozi amapanga mantha kuyenda usika.

b. A Beni ntchito yawo ndi yofotokoza njinga.

c. Maliya akuchapa mbale.

d. Amayi avaya kumsika kukagula ndiwo.

e. Mavuto akuchapa zovala padeni.

2 Konzani ntchito yomwe mungaphunzitse mu Sitandade 4 ndi mayankho oyenera.

3 Fotokozerani anzanu zomwe mwakonza.

4 Zukutani ntchito yomwe anzanu akonza.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Mukonzeretu mayankho a Ntchito 3.
- Muonetsetse kuti ntchito ndi mayankho omwe ophunzira akonza akugwirizana ndi ntchito yomwe apatsidwa.

**Ntchito 4 Kuchita kafukufuku wa mitundu ya mawu**

1 Kambiranani matanthauzo a mitundu ya mawu iyi:

a. dzina

b. mlowam'malo

c. mneni

d. mfotokozi

2 Chitani kafukufuku wa mitundu ya mawu omwe mwapatsidwa.

**3** Fotokozerani anzanu zomwe mwapeza.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Muwapatsiretu ophunzira mitu ya ntchito yomwe afufuze.
- Limbikitsani ophunzira kuti apeze nthawi yapadera yochitira kafukufuku.

**Ntchito 5 Kufotokoza kaphunzitsidwe ndi kayesedwe ka kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo**

1 Kambiranani njira zophunzitsira, zophunzirira ndi zoyesera kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo.
2 Kambiranani ndondomeko yophunzitsira kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo.
3 Lembani zomwe mwakambirana.
4 Fotokozerani anzanu zomwe mwalemba.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Mufufuziretu njira zophunzitsira, zophunzirira ndi zoyesera kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo.
- Mufufuziretu ndondomeko yophunzitsira kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo.

**Ntchito 6 Kusonyeza kaphunzitsidwe ka phunziro la kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo**

1 Unikani njira zophunzitsira, zophunzirira ndi zoyesera kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo.
2 Unikaninso ndondomeko yophunzitsira kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo.
3 Sonyezani momwe mungaphunzitsire phunziro la kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo.
4 Perekani maganizo anu pa ntchito yomwe ophunzira anzanu achita.

**Malangizo kwa mphunzitsi**
Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.

## Kufotokoza mwachidule

M'mutu uno, mwaphunzira kusiyana kwa chiyankhulo cha Chichewa cha m'madera osiyanasiyana komanso kufunika kwa kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo. Mwachita kafukufuku wa mitundu ya mawu. Kenaka, mwafotokoza njira ndi ndondomeko zophunzitsira, zophunzirira ndi zoyesera kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo. Pomaliza, mwasonyeza kaphunzitsidewe ka phunziro la kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo.

## Kudziunika ndi kudziyesa

1 Fotokozani kufunika kwa kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo.
2 Perekani mitundu ya nthawi za aneni.
3 Fotokozani njira ziwiri zophunzitsira, zophunzirira ndi zoyesera phunziro la kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo.

## Matanthauzo a mawu

**Kugwiritsa ntchito malamulo a chiyankhulo** Luso la kutchula, kuyankhula, kuwerenga, kulemba

mawu ndi ziganizo moyenera ndi molondola.

## Mabuku

Malawi Institute of Education (2008). *Maphunziro a m'sukulu zauphunzitsi m'Malawi buku la mphunzitsi*. Domasi: MIE.

Nankwenya, IAJ(2008). *Zofunika mu galamala ya Chichewa*. Blantyre: Dzuka Publishing Company Limited.

Chilora HG & Kathewera REM (2000). *Chinyanja Buku la mphunzitsi la Fomu 1*. Blantyre: Dzuka Publishing Company Limited.

Ngoma SJL& Chauma AM (2011). *Tizame m'Chichewa Malamulo Ophunzitsira ndi ophunzirira Chichewa*. Blantyre: Bookland.

# Mutu 12 Kaphunzitsidwe ka ndagi, nthano ndi sewero

**Luso**: Kuganiza mozama
**Nthawi:** Maola 6
**Chigawo:** Choyamba

## Chiyambi

Munthu aliyense amaganiza. Ngakhale kuti aliyense amaganiza, kuganiza kwathu kumakhala kosiyana ngakhale pa chinthu chimodzi. Mwachitsanzo, pamalo pakagwa vuto, pali anthu ena omwe amasowa chochita pamene ena amatha kuganiza mozama n'kupeza yankho logwira mtima lothetsera vutolo. Kawirikawiri anthu omwe amaganiza mozama amachita zinthu zabwino ndipo amalemekezedwa komanso amadalirika.

Kuganiza mozama ndi limodzi mwa maluso ofunika kwambiri mu phunziro la Chichewa. Ophunzira a kupulayimale ayenera kuphunzitsidwa kuganiza mozama kuti adzakhale nzika zodalirika.

M'mutu uno, muphunzira kufunika kophunzitsa kuganiza mozama kwa ophunzira a m'sukulu zapulayimale ndi kaphunzitsidwe kake.

## Zizindikiro za kakhozedwe

Pakutha pa mutu uno, ophunzira:

- afotokoza ntchito zomwe zingakulitse luso la kuganiza mozama.
- 
- asonyeza kaphunzitsidwe ka ntchito zomwe zingakulitse luso la kuganiza mozama.

## Mawu otsogolera

Kuganiza mozama ndi luso lofunikira kwambiri pa moyo wa munthu aliyense. Anthu ena amaganiza kuti ophunzira saganiza mokwanira. Izi si zoona. Mphunzitsi aliyense ayenera kuzindikira kuti ophunzirawo ali ndi zizindikiro zambiri zomwe zimasonyeza kuti iwo amaganiza mozama. Zizindikirozo ndi izi: kukhala achidwi, kufunsafunsa mafunso, kufuna kuphunzira, kusankha njira zochitira kanthu, kuika zinthu m'magulu kapena m'ndondomeko, kukonda kusewera m'magulu komanso kuchita zisudzo.

Ntchito yaikulu ya mphunzitsi ndi kuthandiza komanso kulimbikitsa ophunzirawa kuti apititse patsogolo luso la kuganiza mozama akadali aang'ono.

**Ntchito 1 Kufotokoza kufunika kwa kuganiza mozama**

1 Kambiranani kufunika kwa kuganiza mozama.
2 Lembani zomwe mwakambirana.
3 Fotokozerani anzanu zomwe mwakambirana.

**Malangizo kwa mphunzitsi**
Mupezeretu mfundo zosonyeza kufunika kwa kuganiza mozama.

**Ntchito 2 Kufotokoza ntchito zomwe zingakulitse luso la kuganiza mozama**

1 Kambiranani mitu ya ntchito zomwe zingakulitse luso la kuganiza mozama.
2 Fufuzani mitu ya ntchito zomwe zingakulitse luso la kuganiza mozama yomwe ikupezeka m'mabuku a Sitandade 1 ndi 2.
3 Fotokozerani anzanu zomwe mwapeza.

**Malangizo kwa mphunzitsi**
Mufufuziretu mitu ya ntchito zomwe zingakulitse luso la kuganiza mozama.

**Ntchito 3 Kufotokoza ndondomeko yophunzitsira ntchito zothandiza kuganiza mozama**

1 Kambiranani ndondomeko zophunzitsira ntchito zothandiza kuganiza mozama izi:
   a. zilapi/ ndagi
   b. nthano
   c. sewero
2 Lembani zomwe mwakambirana.
3 Fotokozerani anzanu zomwe mwalemba.

**Malangizo kwa mphunzitsi**
- Mufufuziretu ndondomeko zophunzitsira ntchito zothandiza kuganiza mozama.
- Musonyeze kuphunzitsa pogwiritsa ntchito ndondomekozi.

**Ntchito 4 Kuonerera kaphunzitsidwe ka ndagi, nthano ndi sewero**

1. Kambiranani mfundo zoyenera kutsatira poonerera phunziro lophunzitsa ndagi, nthano ndi sewero.
   a. Kodi mphunzitsi akutsatira ndondomeko yophunzitsira ndagi, nthano ndi sewero?
   b. Kodi mphunzitsi akuonetsetsa kuti ophunzira akumvetsa zomwe akuphunzira?
   c. Kodi phunziro latenga nthawi yochuluka bwanji?

**Malangizo kwa mphunzitsi**
- Onetsetsani kuti ophunzira akudziwa zoyenera kuchita poonerera phunziro.
- Limbikitsani ophunzira kulemba zomwe akuona.

**Ntchito 5 Kusonyeza kaphunzitsidwe ka ntchito zothandiza kuganiza mozama**

1 Unikani mitu ya ntchito zomwe zingakulitse luso la kuganiza mozama kuchokera m'mabuku a ophunzira.
2 Unikani ndondomeko yophunzitsira ntchito zothandiza kuganiza mozama.
3 Sonyezani momwe mungaphunzitsire ntchito zomwe zingakulitse luso la kuganiza mozama.
4 Zukutani phunziro lililonse.

**Malangizo kwa mphunzitsi**
Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.

## Kufotokoza mwachidule

M'mutu uno, mwaphunzira kufunika kwa kuganiza mozama. Mwafufuza mitu ya ntchito zothandiza kuganiza mozama. Kenaka, mwafotokoza ndondomeko yophunzitsira ntchito zothandiza kuganiza mozama. Potsiriza, mwaphunzitsa ndi kuzukuta phunziro la ntchito zokulitsa luso la kuganiza mozama.

## Kudziunika ndi kudziyesa

1 M'mawu anuanu perekani tanthauzo la 'kuganiza mozama'.
2 Perekani mitu ya ntchito zothandiza kuganiza mozama.
3 Fotokozani momwe ntchitozi zingathandizire ophunzira kuganiza mozama.
4 Fotokozani momwe mungagwiritsire ntchito luso la kuganiza mozama pa moyo wanu wa tsiku ndi tsiku.

## Matanthauzo a mawu

**Kuganiza mozama** kuunika zinthu mwachidwi ndi kusinkhasinkha mwakuya ndi cholinga chofuna kudziwa kapena kupeza choonadi

## Mabuku


Malawi Institute of Education (2006). *Maphunziro a m'sukulu za uphunzitsi m'Malawi Chichewa buku la mphunzitsi*. Domasi: MIE.

Malawi Institute of Education (2015). *Critical thinking training manual for Malawi*. Domasi: MIE.

Malawi Institute of Education (2015). *Malawi primary, secondary and teacher education: critical thinking training manual for Malawi*. Domasi: MIE.

Malawi Institute of Education (2015). *Malawi primary, secondary and teacher education: critical thinking sourcebook for Malawi*. Domasi: MIE.